EXAMINATION NO.:___________________

# THE ALBRIMAS EXAMINATIONS BOARD

**2025 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE 1ST MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Subject Number: P032**
**Time Allowed: 2 hours 15 mins**
**9:30 – 11:45 am**

**Thursday, 20 February**

**Dzina lanu:** ______________________________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** ________________________________________________________

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**
2. Pepela ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D**.
3. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu yanu** pamipata yomwe yaperekedwa.
4. Lembani nambala yanu ya mayeso pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
6. Muchitebulo chili pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake.
7. Perekani kwa oyang'anira mayeso **(imvijileta)** pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 10 | | | |
| 11 – 15 | | | |
| 16 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 – 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 40 | | | |
| 41 - 45 | | | |
| | | | |

**Onani paseri**

© 2025 ALBRIMAS

**Gawo A** (Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso **limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo **kapena** kalata. Mawu a chimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150**.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu "**MTSINJE**" mwa zina tsatani izi polemba

**Ndime yoyamba**

- Komwe mtsinjewo umapezeka
- Komwe mtsinjewo umayambira ndi kuthera

**Ndime yachiwiri**

- Fotokozani kufunika kwa mtsinjewo pamoyo wanu wa tsiku ndi tsiku, pokweza chuma cha dziko ndi poteteza za chilengedwe.

**Ndime yachitatu**

- Fotokozani zomwe mungachite pofuna kuteteza mtsinjewo kuti usadzaume mtsogolomu

**KALATA**

**2.** Lembani kalata kwa mnzanu yomufotokozera mmene mwakonzekera mayeso aboma omwe mulembe chaka chino.

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata
- Mwezi wolembera mayeso

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe mukuchita pokonzekera mayeso
- Thandizo lomwe mukupeza pokonzekera mayeso
- Chiyembekezo chanu pamayesowo

**Ndime yachitatu**

- Momwe mungadzasangalalire mukadzapambana mayeso

**Tsamba loyankhirapo**

Mafunso akupitirira/…

## Gawo B (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

**3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

Kulera ana sikungowayang'anira kuti akudya kapena kuvala bwino kokha, ayi. Pofunika kuwalangiza kuti akule ndi makhalidwe amene angawathandize pamoyo wawo onse, popeza iwowa ndi atsogoleri a mawa. Nawonso ayenera kudzathandiza ana awo m'tsogolo muno.

Kawirikawiri ana amaphunzira bwino ndi zitsanzo osati mawu okha.Ngati tiuza ana kuti adzifika pakhomo dzuwa lisanalowe pafunika kuti tionetsetse kuti ifenso makolo tidzifika nthawi yabwino. Ngati makolo auza ana kusachita zomwe iwo akuchita zimakhala zovuta kumvera chifukwa ndi chinthu chosamveka kwa mwana kuti asachite zoterozo pamene akuona makolo akuchita zomwezo.

Sibwino kumuopseza mwana amene walakwa zomwe sungachite, monga kunena kuti ndidzakupha pamene tikufuna kuti asinthe chifukwa amazindikira kuti ndizonama, choncho iye amapeputsa malangizo operekawo. Ngati mwana walakwa tiyeni timulangize nthawi yomweyo ndipo moyenera.

Mwana akalakwa pakhomo, abambo ena amakalipira amayi, amvekere, "Tawona zimene mwana wakoyu akuchita!" Kodi wasanduka mwana wa mayi yekha chifukwa walakwa?

Makolo enanso sadziwa kulanga ana monga m'mene ayenera kuchitira, ena ngakhale mwana alakwe chotani, sakalipa ayi, amangoyang'ana. Kodi zimenezi zibzala chiyani mwa mwanayo? Chofunika ndi chakuti makolo asonyeze udindo wawo polanga ana akalakwa chifukwa akapanda kutero anawo sakula ndi makhalidwe abwino.

Pamene mwana walakwa muitaneni ndi kumudzudzula nthawi yomweyo. Muthanso kumukwapula ndi kachikwapu kakang'ono osati chachikulu ayi. Zimenezi ziyenera kuchitika nthawi yomweyo imene mwanayo walakwa. Pamenepa mwana amazindikira kuti akulangidwa chifukwa cha zomwe walakwa. Ana ena okulirapo ayenera adzudzulidwe paokha osati pamene pali ana ang'ono. Koma tikangomuyang'ana amaganiza kuti kukhala ndi kumeneku. Tiyeni tidzudzule pakaoneka cholakwa osangoyang'anira popeza muvi woyang'anira suchedwa kulasa m'maso.

Mafunso akupitirira/…

Pali ana ena omwe ndi ankhutukumve, amangokhala ngati adalodzedwa. Ngakhale alangizidwe, iwo amangobwerezabe zolakwazo. Ana otere tisatope nawo, koma tiyenera kuwalangizabe chifukwa ngakhale avute ali m'manja mwathu.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa:**

a. Kodi atsogoleri a mawa ndi ndani?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. N'chifukwa chiyani atsogoleri a mawa ayenera kulangizidwa?

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

c. Perekani zitsanzo ziwiri zomwe makolo angachite poonetsa makhalidwe abwino.

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

d. N'chifukwa chiyani makolo ayenera kuphunzitsa ana ndi zitsanzo pakhomo osati ndi mawu okha?

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

e. Kodi mwana amadziwa bwanji kuti zimene akumulangiza n'zowona?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

f. Ndi mavuto awiri ati omwe amayi amatha kukumana nawo mwana akalakwa?

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

g. Kodi mwini wa ana pakhomo ndani?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

h. N'chifukwa chiyani ana ena sakula ndi makhalidwe abwino?

________________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

i. Kodi ndi nthawi yanji yomwe mwana ayenera kulangidwa akalakwa?

________________________________________________________________

**(Malikisi 1)**

j. Pezani mawu m'nkhaniyi omwe akutanthauza:

   i. "ana osamva"

   ____________________________________________________________

   **(Malikisi 1)**

   ii. "kungokhala osachita kanthu"

   ____________________________________________________________

   **(Malikisi 1)**

k. Kodi makolo ayenera kuchita chiyani ngati ana akupitirizabe kulakwa?

________________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

l. Perekani mutu wa nkhaniyi.

________________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

## **GAWO C** (Malikisi 10)

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.
"Pepani anthu onse mwafika pano. Tsopano ndi nthawi yoti tiyambe mwambo woperekeza mfumu yathu yagona apayi."

**Mafunso**

i. Kodi malonjewa angaperekedwe pa mwambo wanji?

______________________________________________________________

**(Malikisi 1)**

ii. Lembani udindo wa munthu amene angapereke malonjewa.

______________________________________________________________

**(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

iii. Kodi mawu oti “Mfumu” akutanthauzanji?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

iv. Tchulani zinthu ziwiri zofunika pamsika pofuna kupititsa ukhondo patsogolo.

_______________________________________________

_______________________________________________

**(Malikisi 2)**

**5. Kupanga ziganizo**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. njenjemera

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. mlendo

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

c. du

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

d. chola

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

e. zemba

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

**GAWO D** (Malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza (**A, B, C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**6.** Mwana wosamva amachititsa manyazi makolo.
A. mfotokozi
B. muonjezi
C. mneni
D. mlumikizi

**7.** Mlangiziyo wachokera ku unduna wa zaulimi.
A. mlowammalo
B. mlumikizi
C. mneni
D. mperekezi

**8.** Iye amavina mogometsa paukwati.
A. mfotokozi
B. mvekero
C. muonjezi
D. mneni

**9.** Jonasi wagwa kuti khu.
A. mperekezi
B. mvekero
C. mfuwu
D. muonjezi

**10.** Ophunzira okonda kujomba amalephera mayeso.
A. mfotokozi
B. dzina
C. mneni
D. mlowammalo

**Mafunso 11 mpaka 15:** Sankhani mitundu ya mayina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**11.** Ndiwo zonse anadya ndi Lozani.
A. dzina la chinthu chosakhudzika
B. dzina lopanda mwinimwini
C. dzina la chinthu chokhudzika
D. dzina la mwinimwini

**12.** Mwano supindula.
A. dzina la chinthu chokhudzika
B. dzina la mwinimwini
C. dzina la chinthu chosakhudzika
D. dzina lopanda mwinimwini

**13.** Wataya madzi ambiri.
A. dzina la chinthu chokhudzika
B. dzina launyinji
C. dzina la mwinimwini
D. dzina la chibale

**14.** Msambi wankhosa walowa m'munda mwathu.
A. dzina la chinthu chosankhudzika
B. dzina lopanda mwinimwini
C. dzina la mwinimwini
D. dzina launyinji

**15.** Nyani wadya chimanga m'dimba lawo.
A. dzina la chibale
B. dzina lopnda mwinimwini
C. dzina launyinji
D. dzina la chinthu chosakhudzika

**Mafunso 16 mpaka 20:** Sankhani mitundu ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**16.** Watenga kawiri kokha.
A. wa malo
B. wa mchitidwe
C. wa nthawi
D. wa chiwerengero

**17.** Bwera kuno.
A. wa mchitidwe
B. wa nthawi
C. wa malo
D. wa chiwerengero

**18.** Mtsikanayo abwera mawa.
A. wofunsa
B. wotsimikiza
C. wa nthawi
D. wa mchitidwe

**19.** Iye amavina mothimbwidzika.
A. wa maonekedwe
B. wa mchitidwe
C. wa chiwerengero
D. wofunsa

**20.** Mwayika kuti mabuku aja?
A. wofunsa
B. wa malo
C. wa mchitidwe
D. wobwerezabwereza

**Mafunso 21 mpaka 25:** Sankhani msintho wa aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**21.** Vinani bwino, mukuthirana madzi.
A. wochititsitsa
B. wamchibisira
C. womchitira
D. wochitirana

**22.** Mwanayo wakanitsitsa kubwera kuno.
A. wochitirana
B. wochititsitsa
C. womchitira
D. wochitidwa

**23.** Njoka yolusa ija yaphedwa dzulo.
A. womchitira
B. wochitirana
C. wochitidwa
D. wochititsa

**24.** Bwanawe tiye tikapondeponde kaye podikira nthawi.
A. wobwerezabwereza
B. wochititsa
C. wochitidwa
D. womchitira

**25.** Mtsikana wamwano uja wamenywa.
A. wochitirana
B. wotsutsana
C. wochitidwa
D. wonyazitsa

**Mafunso 26 mpaka 30:** Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**26.** A Mbewe adakolora mawere ochuluka.
- A. nsawawa
- B. mapira
- C. nandolo
- D. lipoko

**27.** Ife kwathu tafunditsa mkute.
- A. tasisimitsa
- B. tagawa
- C. taphika
- D. tatenthetsa

**28.** Chipupa ichi ndi cholimba.
- A. khoma
- B. denga
- C. mzati
- D. nsichi

**29.** Munthu wamanjalende amavutika.
- A. wolimba
- B. waulesi
- C. wokongola
- D. wakuba

**30.** Yankho ndi mzime m'banja mwathu.
- A. woyamba
- B. wachiwiri
- C. womaliza
- D. wachisamba

**Mafunso 31 mpaka 35:** Sankhani matanthauzo a zining'a zotsatirazi.

**31.** Kuyankhulira nsonga ya lirime.
- A. chibwibwi
- B. kulalata
- C. kunyoza
- D. kunyada

**32.** Chidameta nkhanga mpala.
- A. kukhaula
- B. kuchita tsoka
- C. kumeta
- D. kusosola nkhanga

**33.** Maliro m'mbale.
- A. nsomba
- B. nyemba
- C. nyama
- D. mfutso

**34.** Kugwa nkhope.
- A. kunyengelera
- B. kuchita mantha
- C. kuchita manyazi
- D. kuchita chisoni

**35.** Waziwala m'maso.
- A. wopenga
- B. wokwiya
- C. wovuta
- D. wozindikira

**Mafunso 36 mpaka 40:** Sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo yomwe ili ndi mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.

**36.** Kuti ndinu a mwano ndi zoona.
- A. yamuonjezi
- B. yadzina
- C. yoima payokha
- D. yamfotokozi

**37.** Tidalemba chimangirizo monga adatiuzira.
A. yadzina
B. yamuonjezi
C. yamfotokozi
D. yoima payokha

**38.** Wagula njinga yamoto poti amasilira ya anzake.
A. yamuonjezi
B. yamfotokozi
C. yadzina
D. yoima payokha

**39.** Ng'ombe yomwe yaphedwayo ndi yanga.
A. yoima payokha
B. yadzina
C. yamuonjezi
D. yamfotokozi

**40.** Sitidaulure zomwe tidagwirizana.
A. yadzina
B. yamuonjezi
C. yoima payokha
D. yamfotokozi

**Mafunso 41 mpaka 45:** Sankhani ntchito za **"ndi"** m'ziganizo zotsatirazi.

**41.** Mtolo wa nkhuni uli ndi.
A. mlumikizi
B. mlowammalo
C. mvekero
D. mperekezi

**42.** Ndilemba mayeso chaka chino.
A. mlowammalo
B. mperekezi
C. mvekero
D. mneni

**43.** Ana ali ndi makolo awo.
A. mlowammalo
B. mperekezi
C. mvekero
D. mlumikizi

**44.** Ulimi wa ziweto ndi wabwino.
A. mlumikizi
B. mneni
C. mlowammalo
D. mperekezi

**45.** Ine ndimakonda mzimbe, mango ndi nthochi.
A. mneni
B. mlumikizi
C. mlowammalo
D. mperekezi

**MAFUNSO ATHERA APA**

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikiza khumi ndi awiri.**

**ALBRIMAS** (Alipo Schools, Bright Future, Maranatha Institute, Snow White Schools & Word Alive Christian Academy)

***Excelling together!!!!!***
Monsieur FrancisNHO Productionz ©
**0999 86 47 05**